80-Ndipo mwanayo anakula komanso anali olimba mu uzimu,ndiponso anali mu chipululu mpaka mu nthaŵi imene anawonekera ku khamu la a Isirayeli.

-Yohane ankakhala mu chipululu mpaka pa nthaŵi imene Mulungu anamuyitana iye kuti aŵawonetse njira anthu.



## PHUMZIRO LA 44

1. Kodi chinamuchitikira ndi chiyani Zakariya pamene anali Mnyumba ya Mulungu ija?
-Mngelo wa Mulungu anamuwonekera Zakariya.

2. Kodi mngeloyo anamuwuza chiyani Zakariya?
-Mngeloyo anamuwuza Zakariya kuti Mulungu ankafuna kumupatsa iye mwana wamamuna, ndipo dzina lake lidzakhala Yohane.

3. Kodi kenako mngeloyo analankhula chiyani za mwana wamamuna amene Mulungu ankafuna kumupereka kwa Zakariya uja?
-Mngeloyo analankhula kuti mwana wamamuna wa Zakariya, Yohane, adzaŵapangitsa anthu kukhala okonzeka pomudikilira Mpulumutsi amene ankabwerayo.

4. Kodi mngeloyo anamutcha kuti ndani Mpulumutsi amene ankabwerayo?
-Ambuye.

5. Kodi Ambuye ndi ndani?
-Ambuye ndi Mulungu.
-Mngeloyo analankhula kuti Mpulumutso amene ankabwerayo adzakhala Ambuye, Mulungu mwini.

6. Kodi mngelo anamuwuza chiyani Maliya?
-Mngelo anamuwuza Maliya kuti Mulungu anamusankha iye kuti akhale mayi wa Mpulumutso amene ankabwerayo.

7. Kodi dzina la mwana wa Mariya lidzakhala ndani?
-Yesu.

8. Kodi dzina lakuti “Yesu” likumasulira chiyani?
-Dzina lakuti “…Yesu” likumasulira kuti “Mpulumutsi”.

9. Kodi mngeloyo ankamasulira chiyani pamene ankanena kuti mwana wamamuna wa Mariya adzatchedwa kuti Mwana wa Wakumwamba?
-Mwana wamamuna wa Mariya adzakhala Mwana wa Mulungu.

10. Kodi zidzatheka bwanji kuti mwana wamamuna wa Mariya kuti adzakhale Mwana wa Mulungu?
-Mulungu Atate ndi Mulungu Mzimu Oyera ankamutumiza Mulungu Mpulumutsi pa dziko la pansi ngati Mwana wa Mulungu komanso mwana wa munthu.

11. Kodi Mwana wamamuna wa Mariya adzakhala Mulungu komanso munthu?
-Inde.

12. Kodi chifukwa chiyani mwana wamamuna wa Mariya anakabadwa palibe mbewu ya mamuna ndi mkazi?
-Chifukwa chakuti Iye ankafunika kuti abadwe alibe tchimo la Adamu ndi Hava.
-Chifukwa chakuti Iye ankafunika kuti abadwe ali olungamika ndiponso opanda tchimo.

13. Yesu anakhala Mpulumutsi amene Mulungu analonjeza kwa Abulahamu, Isaki, Yakobo ndi anthu onse?
-Inde.

-Nthaŵi yakuti Elizabeti, mkazi wache wa Zakariya, akhale ndi mwana, inafika.

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:57-58

57-Tsopano nthaŵi yinakwana yakuti Elizabeti abereke, ndipo anabereka mwana wamamuna.
58-Anansi ndi abale ache anamva kuti Ambuye



-Apa pali chitsanzo:
-Tsiku lina usiku kwambiri, kulibe kuwala kwa mwezi ndi nyenyezi, inu mukusochera mu thengo losadziŵika.

-Inu powuwopa mdima, mumadikira kuwala kwa dzuŵa kuti kutuluke kaye m'maŵa.

-Adamu ndi Hava  atachimwa, iwowo anasiyidwa ndi Mulungu, amene anali kuwala kwa miyoyo yawo.

-Chifukwa cha machimo awo, anthu onse anabwadwira mu mdima wa Satana.

-Mpulumutsi adzabwera kudzapereka kuwala pakutha kwa mdima wa Satana ngati m'mene limaperekera kuwala dzuŵa, mdima ukatha.

-Kodi pali dzuŵa lingati pa dziko la pansi pano?
-Limodzi.
-Pali Mpulumutsi m'modzi yekha ngati m'mene lilili dzuŵa pa dziko la pansi pano
-Mpulumutsi m'modzi yekhayo akutheka kupulumutsa anthu onse pa dziko la pansi pano ngati m'mene limaperekera kuwala dzuŵa limodzi lokha pa dziko la pansi.

-Mulungu sanalonjeze kuti adzatumiza Apulumutsi ambiri, ayi.
-Mulungu analonjeza zakuti adzatumiza Mpulumutsi m'modzi yekha.

-Yohane mwana wamamuna wa Zakaliya, anakula, ndipo anamukhulupilira kwambiri Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:80

-Kodi ndani yekha amene anamupulumutsa Yona m'mimba mwa msomba yayikuru ija?
-Mulungu.

-Mulungu yekha ndi amene angathe kutipulumutsa ife ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Zakaliya za mwana wache wamamuna, Yohane?

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:77

77-Zakaliya analankhula kuti, "kuŵadziŵitsa anthu ache za chipulumutso poŵakhulukira machimo awo."

-Zakaliya analankhula kuti Yohane adzaŵawonetsa anthu njira yopulumukira.

-Zakaliya analankhula kuti Yohane adzaŵawonetsa anthu njira ya machimo awo kuti adzalipilidwe.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Zakaliya?

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:78-79

78-Zakaliya analankhula kuti, "Kudzera mu chisoni cha Mulungu chimene chikutisamalira ife, adzatitumizira kuwala kwa chipulumutso chachikulu kuchokera kumwamba ngati kutuluka kwa dzuŵa,
79-kukubwera kuti kupereke kuwala kwa amene akukhala mu mdima ndi nthuzi wa imfa, kudzatitsogolera ife ku njira ya moyo yobweretsa mtendre."

-Kodi Mpulumutsi amene akubwerayo adzakhala bwanji ngati dzuwa limene likuturuka?



amuchitira chisoni chachikuru ndipo anasangalala naye pamodzi.

-Kodi Mulungu anasunga lonjezo lache kwa Zakaliya ndi Elizabeti loŵapatsa mwana wamamuna?
-Inde.

-Mulungu anapereka mwana wamamuna kwa Zakaliya ndi Elizabeti, ndipo iwowo anamutcha dzina lakuti Yohane.

-Pamene Yohane, mwana wamamuna wa Zakaliya anabadwa, Mulungu Mzimu Woyera analankhula kudzera mwa Zakaliya.

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:67-71

67-Zakaliya, bambo wa mwanayo, anadzadzidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo Mulungu analankhula kudzera mwa iye kuti,
68-"Ulemelero upite kwa Ambuye, Mulungu wa a Isirayeli, pakuti afika kudzakuthandizani , kudzakupulumutsani ndipo kwamasula anthu amene anaŵasankha.
69-Ndipo mutikwezere amene ali ndi mphamvu, amene adzatipulumutse ife wa mbewu ya DaElizabetide mtumiki wache."

-Kodi Zakaliya ankalankhula chiyani?
-Zakaliya amkamupembedza Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani Zakaliya amkamupembedza Mulungu?
-Chifukwa chakuti Zakaliya ankadziŵa kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi posakhalitsa.
-Chifukwa chakuti Zakaliya ankadziŵa kuti Mpulumutsi adzabwera kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.

-Anthu onse akufunidwa kuti apulumutsidwe ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.

-Ichi ndi chifukwa chimene Mulungu anamutumizira Mpulumutsi pa dziko la pansi pano.

-Kodi Zakaliya anadziŵa bwanji kuti Mpulumutsi adzabwera kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana?
-Chifukwa chakuti Zakaliya anaŵerenga mu buku la Mulungu limene analonjeza zotumiza Mpulumutsi.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Zakaliya?

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:72-75

72-Zakaliya anati, "Kuti awonetse chisoni chimene anapangana nawo makolo athu, ndikusunga pangano lake loyera,
73-malumbilo amene analumbila kholo lathu, Aburahamu,
74-kutilora kuti, akadzatipulumutsa ku mphamvu ya adani athu, tidzatha kuŵatumikira mosawopa,
75-tili oyera ndikulungamika pa maso pache kwa masiku onse a moyo wathu."

-Zakaliya anadziŵa kuti Mulungu akhala akusunga pangano lache lotumiza Mpulumutsi.

-Ili linali lonjezo limene Mulungu anapereka kwa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo mu zaka zambiri zapitazo.

-Mulungu amasunga malonjezo ache.
-Mulungu saphwanya malonjezo ache.



-Kodi Zakaliya analankhula chiyani za Yohane, mwana wache wamamuna amene anabadwa mwa iye?

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:76

76-Zakaliya anati, "Ndipo iwe, mwana wanga udzatchedwa kuti Mneneri wa Wakumwamba Kwambiri; pakuti udzapita patsogolo pa Ambuye kukakhonza njira zawo."

-Zakaliya anati kuti Yohane mwana wache wamamuna adzakhala Mneneri wa "Wakumwamba Kwambiri."

-Kodi "Wakumwamba Kwambiri" ndi ndani?
-Mulungu Atate.

-Kodi tchito ya mwana wamamuna wa Zakaliya, Yohane, idzakhala yotani?
-Yohane adzakhala patsogolo pa Ambuye, kwakhozera njira lwowo.

-Kodi Ambuye amene adzaŵakhonzere njira Yohanewo, anali ndani?
-Anali Yesu, Mulungu Mpulumutsi.

-Kodi ndani yekha amene anamupulumutsa Nowa ndi banja lake ku chigumula cha madzi?
-Mulungu.

-Kodi ndani yekha amene anamupulumutsa Isaki ku imfa ndikupereka mkhosa m'malo mwache?
-Mulungu.

-Kodi ndani yekha amene anaŵapulumutsa a Isirayeli mu ukapolo wa Falawo?
-Mulungu.